JW.ORG™

Koperani nkhaniyi pa www.jw.org

Anthu Akhate Anafunika Kuchiritsidwa

Matenda a khate amatchulidwa m'Baibulo kambirimbiri. (2 Mafumu 5:1; Luka 5:12-14) Kodi matenda amenewa anali otani? N'chifukwa chiyani anthu akhate ankafunikira kwambiri kuchiritsidwa?

Inuyo pamodzi ndi banja lanu, fufuzani kuti mudziwe zambiri zokhudza matenda amene Baibulo limatchula kuti khate. Mungagwiritse ntchito buku lachingelezi la *Insight on the Scriptures* (lomwe likupezekanso m'zinenero zambiri pa jw.org pamene alemba kuti PUBLICATIONS > ONLINE LIBRARY) kapena mungagwiritse ntchito mabuku ena amene alipo m'Chichewa.

Aisiraeli omwe anali ndi khate ndiyeno n'kuchiritsidwa, ankafunika kuchita mwambo winawake asanabwerere mumzinda n'kuyamba kukhala ndi anthu ena. Werengani Levitiko 14:2, 4, 8, 10, 20, kenako lembani manambala pazithunzi zimene zili m'munsizi mwandondomeko imene munthu amene wachiritsidwa khate pamodzi ndi wansembe anafunika kutsatira.

▶ **TAYESANI IZI:** Werengani Luka 5:12-15 kuti mudziwe mmene Yesu ankachitira zinthu ndi anthu akhate amene ankakumana nawo. Kenako lembani maina a anthu amene mukuwadziwa omwe akudwala matenda aakulu. Kambiranani zimene mungachite potsanzira Yesu pa nkhani yosonyeza chifundo kwa anthuwo.

Mayankho: **1.** Munthu yemwe wachiritsidwa ku matenda a khate akupitisidwa kwa wansembe. **2.** Wakhate akubwereta mbalame ziwiri. **3.** Wakhate akuchapa zovala zake. **4.** Wakhate wateng'a nkhosa ziwiri zamphongo ndi mwana wankhosa mmodzi. **5.** Wansembe akuperekа nsembe.

www.jw.org © 2013 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania